

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO KUPITA
KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

MKAZI WOVEKEDWA DZUWA

"Ndipo chizindikiro chachikulu chinaoneka m'mwamba; mkazi wovekedwa duwa, ndi mwezi kumapazi ake, ndi pamutu pake korona wa nyenyezi khumi ndi ziwiri" (Chivumbulutso 12:1).

Mtumwi Yohane anali ndi mwayi woona masomphenya a ulemerero a mkazi uyu amene anali kumwamba, ali mu kuwala konyemizira ndi koonekera. Masomphenya amene alembedwa mu buku la Chivumbulutso akunenedwa mwa chifanifani pofuna kuonetsera zoonadi zofunikira. Mwachithunzithunzi, mkaziyu akuyimira mpingo – kaya mpingowyo ndi wachinyengo kapena woona. Mu masomphenya awa, mkaziyu akuonetsedwa ngati woyerape popeza wavekedwa duwa. Iye akuyimira chiyero ndi ulemerero wa mpingo umene wamangidwa pa chiphunzitsio cha atumwi. Izizikusiyana kwambiri ndi mpingo wachinyengo umene ukuyimira mkazi wachierewere amene akuonetsedwa m'masomphenya monga mkazi amene ndi wosakhulupirika kwa mwamuna wake.

Mkazi amene ali m'masomphenyayu anaima pa mwezi. Mwezi paokha ulibe kuwala ndipo kuwala kwake kumachokera ku duwa. Mwezi ndi chizindikiro cha mu Chipangano Chakale chimene chinali

"chifaniziro chenicheni cha zinthuzo" (Ahebri 10:1). Panganolo linali ngati mkulu wa sukulu kapena mphunzitsi kuti



Mpingo wa Mulungu Waulemelero

litifikitse ife kwa Khristu (Agalatiya 3:24-26). Ilo limalozena ku zabwino zimene zili nkudza. "Chifukwa chilamulo chinapatsidwa mwa Mose; chisomo ndi choonadi zinadza mwa Yesu Khristu" (Yohane 1:17).

Mkaziyo anavekedwa ndi ulemerero wa duwa. Dzuwa limaperekwa kuwala kwake kuchokera kumwamba. Panali kuwala kokongola kwa choonadi kumene kunathamangitsa mdima pamene Khristu anabwera ku dziko lino lotayikali. Khristu ndiye gwero la kuwala kwauzimu mu dongosolo la Chipangano Chatsopano. Kuwala kwa choonadi kumafulula uchimo ndi kulozera ku njira ya chilungamo ndi chigonjetso. Mpingo woona umavekedwa ndi kuwala kwa ulemerero wa chiyero ndipo umaposa kuwala kwa chizimezime ndi kosaoneka bwino kwa mu Chipangano Chakale.

Mkaziyo anali ndi korona wa nyenyezi 12 pamutu pake. Koronayo akuyimira ulamu-liro ndiponso mphamvu ya kulamulira. Mpingo wa Mulungu sugonjetsedwa kapena kumangidwa mu unyolo ndi uchimo koma ukulamulira mogonjetsa mphamvu zonse za mdani, ngakhale mu nyengo ino imene ili yoipa.

Mtumwi Yohane pachiyambi anaonetsewa masomphenya a "nyenyezi zisanu ndi ziwiri ndi ...zoikapo nyali zisanu ndi ziwiri" (Chivumbulutso 1:20). Iye anauzidwa kuti nyenyezizo zinali angelo a ku mipingo yokwana isanu ndi iwiri. Choncho

(Yapitirira pa tsamba 2)

Mau a Mkonzi

Tsamba 3

Kusanthula Mau a
Mulungu:
Mpingo wa Mulungu

Tsamba 4

Nkhani yotsagana nayo:
Mpingo wa Mulungu

Tsamba 5

Mafunso ndi Mayankho:
Mpingo wanga suphunzitsa choonadi...

Tsamba 7

Kodi Mukudziwa?

Mau a pa Nyengo yake

Tsamba 8

zimene **BAIBULO** limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyeria

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akor. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhazidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba I)

nyenyezizo zikuyimira atumiki amene akunenedwa kuti ndiwo ‘angelo’, kapena onyamula uthenga. Nyenyezi 12 zija zimene zinali pa korona wa mkazi uja zikhoza kukhala utumiki umene umanyamula uthenga wabwino ku dziko lotaikali. Amene amadziwika bwino pakulalikira uthenga wabwino mu mpingo woyamba anali atumwi 12 aja. Iwo anavutika kuyambira pachiyambi chifukwa cha kulalikira za kuwala kwa choonadi. “Pamenepo ndipo simulinso alendo ndi ogonera, komatu muli a mudzi womwewo wa oyera mtima ndi a banja la Mulungu; omangika pa maziko a atumwi ndi aneneri, pali Khristu Yesu mwini, mwala wa pangodya” (Aefeso 2:19-20).

Mipingo yambiri ndi zipembedzo zochuluka achita tchimo la chigololo cha muuzimu nachita chiwerewere ndi zinthu za dziko lino. Mipingo ikugwadira mafano a nthawi ino ndipo ikuvomereza ziphunzitso ndi zikhaldidwe zauchimo. Zikhulupiriro za anthu zikutenga malo kuposa Mau a Mulungu. Mipingo imeneyi singakhale yokhulupirika kwa mkwatibwi, Yesu Khristu.

Mipingo woona wa Mulungu unatomeredwa kwa mwamuna mmodzi ndipo udzaperedwa kwa Khristu ngati namwali wangwi (2 Akorinto 11:2). Ndi chofuna cha Ambuye “kuti lye akadziikire yekha Mipingo wa ulemerero, wopanda banga, kapena khwinya, kapena kanthu kotere; komatu kuti akhale woyeria, ndi wopanda chilema” (Aefeso 5:27). Tiyamika Mulungu chifukwa cha mkwati wokongola wa Khristu amene wadzisunga mwachiyero ndi osadzidetsa, ndipo avala kuwala ka ulemerero wa Mau a Mulungu.

-mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choondi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata yuu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoona za Baibulo zimene zakhzakitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumut-so ndi mamaslidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maomboledwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwe ndi Mzimu Woyeria kumene kumatasirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, twongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gavo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

KUTI MULANDIRE Nawo Kalatayi

Uthenga Wabwino wa Choondi ndi uthenga wa kalata umene timesindikiza miyezi itatu illyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choondi imasindikizidwa mu maiko osianasiyana kuti igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zoperekwa zafulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, 605 Bishops Ct., Nixa, MO 65714 USA

editor@thegospeltruth.us

Mau a Mkonzi



"Chifukwa cha Ziyoni sindidzakhala chete, ndi chifukwa cha Yerusalemu sindidzapuma, kufikira chilungamo chake chidzatuluka monga kuyera, ndi chipulumutso chake monga nyali yoyaka" (Yesaya 62:1).

Phunziro la ulendo uno lagona pa mutu wa ‘Mpingo’. Chokhumba cha mtima wanga ndicho chakuti munthu aliyense woyerwa mtima akhale ndi masomphenya a kukongola kwa mpingo weniweni wa Mulungu. Mabungwe ambiri a Chikhristu apeputsa kwambiri choonadi koteru kuti anthu saonanso kufunikira kwake “konyamula mtanda wao tsiku ndi tsiku” monga mmene Ambuye anaphunzitsira. Kutumikira Ambuye ndi njira yopapatiza komanso yachiyero komabe ili njira yabwino. Iyi ndi njira imene imatsogolera ku mphamvu ndi chigonjetso. Tikalola choonadi cha Mau a Mulungu kuti chikhale mmoyo wathu ndiponso chiyanjano, izi zimabweretsa mtendere ndi kumasuka pa kupembedza mu “mzimu ndi mu choonadi.”

Anthu ambiri safuna kuvomereza kuti iwo ali gawo limodzi la mpingo wa munthu, koma pamene tikuphunzira malemba, ndipo zimakhala zoonekeratu kuti mipinga yambiri sili gawo la mpingo weniweni wa Mulungu umene uli umodzi. Mulungu anayikiratu momveka bwino dongosolo la Mpingo Wake. Si ntchito yathu kuzisinthia kapena kukonzango zimenezi. Udindo wathu ndiwo kudziyesa ngati tikuchita molingana ndi Mau a Mulungu. Mpingo wa Mulungu ndi wokongola ndi waulemelero. Monga phiri la Ziyoni, umakwera pamwamba pa mitambo ya chisokonezo imene imafuna kulowerera dziko la chipembedzoli.

Kumasuka ku uchimo ndi mdalitso, komanso kumasuka ku zikhulupiriro ndi ziphunzitso za anthu ndi mdalitso winanso. Si kokwanira kungokhala ndi chidziwitso cha choonadi chimenechi. Nzofunika kuzichita kuti potero thupi la Khristu lisungike losadetsedwa. Mipinga yambiri imadzitcha kuti ndiyo ‘Mpingo wa Mulungu’, koma dzina lokhalo silikwanira. Kodi Mzimu wa Mulungu akuwatsogolera kapena ndi munthu amene akulamulira. Kodi ndiwo muyeso wa chikhulupiriro chathu kapena timangotenga zimene abusa anena? Kodi pali anthu amene amatengedwa kuti ndiye eni mpingowu kapena Khritu ndiye mutu wa mpingo wanu? Ambuye atithandize kuti tife ku undekha wathu ndipo kuti mpingo ukadziwikedu kuti ndiwo ‘Mudzi womangidwa pamwamba pa Phiri’ umene sungathe kubisika.

Tiyenera tidzipereke osati ku mbiri yakale kapena chikhaldwe chathu. Anthu ambiri ngakhale a mu ‘Mpingo wa Mulungu’ ali mu mpingowu chifukwa anabadwira ndi kukulira mmenemo. Zimatengera kusinthika kwa mtima kochokera kumwamba kuti munthu akhale mu Mpingo wa Mulungu. Tiyenera tidzipereke kwa Mulungu Mwini ndi kwa Mau ake ndipo izi zidzatipangitsa kuti tsiku ndi tsiku tiyende mmoyo wachiyero.

Monga mmene Ambuye angatsogolere, ndidzakamba za umodzi komanso chiyanjano mu makalata akutsogolowa.

Khala wokhulupirira mzanga, popeza Ambuye akubwera posachedwapa.

Michael W. Smith

October 2013

Zambiri Zilî pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza
pa intaneti, mulembe
www.thegospeltruth.us
kuti mudzilandira
makalata athu kapenango
kuti muone makalata
akale.



Thupi

Mzimu

Chiyembekezo

Mbuye

Chikhulupiriro

UBATIZO

MULUNGU

Atate

Chiphunzitso

DZINA

Aefeso 4:4-5

2 Timoteo 3:16-17

Aefeso 3:14-15

KALOZERA POSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU: MPINGO WA MULUNGU

Malemba: Ndipo Ambuye anawaonjezera tsiku ndi tsiku amene akuti apulumutsidwe..

Machitidwe 2:47

Kuomba mkota: Mpingo ndi bungwe lakumwamba limene linakhaziktisidwa ndi Yesu, motso-gozedwa ndi Mzimu Woyeru, ndipo Mau a Mulungu ndiwo muyeso wolamulira chikulupiriro. Mpingo wa M'baibulo — Mpingo wa Mulungu, wapangidwa ndi okhulupirira onse amene anapulumutsidwa ku machimo awo.

Tanthauzo: Mau akuti 'mpingo' akuchokera ku mau a chi Griki akuti 'ekklesia' amene amanta-nthauza 'gulu' kapena 'kuitana'.

I. Wokhazikitsa ndi Womanga

- A. Mateyu 16:15-18 Wamangidwa pa Khristu.
- B. Ahebri 8:1-2 Wosamangidwa ndi munthu.

II. Maziko ndi Khomo —Yesu

- A. 1 Akorinto 3:9-11 Maziko.
- B. Aefeso 2:20 Mwala wapangodya.
- C. Yohane 10:7-9 Khomo lokhalo la ku chipulumutso.

III. Anthu ake

- A. Machitidwe 2:46-47 Onse opulumutsidwa.
- B. 1 Akorinto 1:2 Oyera mtima.
- C. 1 Akorinto 12:18 Mulungu amaika ma membala mu thupi.
- D. 1 Yohane 5:18 Anthu ake sachimwa.

IV. Buku la umembala

- A. Luka 10:20 Maina alembedwa m'buku la Kumwamba.
- B. Afilipi 4:3 Buku la Moyo. (Chivumbulutso 20:12).

V. Mutu wake—Khristu

- A. Aefeso 1:22 Mutu pa zinthu zonse.
- B. Aefeso 5:23-24 Mutu wa Mpingo. (Aefeso 4:15-16)
- C. Akolose 1:17-19 Mutu was thupi.
- D. Yesaya 33:20-22 Oweruza ndi opereka lamulo.

VI. Lamulo la Chikhulupiriro

- A. 2 Timoteo 3:16-17 Malemba onse.
- B. 2 Petro 1:21 Anauziridwa ndi Mulungu.

VII. Dongosolo lake

- A. 1 Akorinto 12:18, 27-28 Mulungu amaika anthu mu mpingo.
- B. Aefeso 4:10-13 Mulungu amapereka mphatso.
- C. 2 Akorinto 3:5-6 Mulungu amapereka atumiki.

VIII. Dzina lake kuchokera mu Baibulo

- A. Aefeso 3:14-15 Umanenedwa kuchokera kwa Atate.
- B. Machitidwe 20:28 Dyetsa Mpingo wa Mulungu.
- C. 2 Akorinto 1:1 Mpingo wa Mulungu ku Korinto. (1 Atesalonika 2:14)

IX. Mpingo umodzi

- A. Aroma 12:4-5 Thupi limodzi mwa Khristu.
- B. Aefeso 4:4-6 Chikhulupiriro chimodzi.
- C. 1 Akorinto 12:12-14, 20 Ziwalo zambiri komabe thupi limodzi.

X. Zizindikiro za Mpingo

- A. Aefeso 1:22-23 Thupi la Khristu.
- B. 2 Akorinto 11:2 Mkwatibwi wa Khristu.
- C. Ahebri 12:22-23 Mzinda wa Mulungu -- Phiri la Ziyoni.
- D. 1 Timoteo 3:15 Nsanamira nd Mchirikizo wa Choonadi.

MPINGO WA MULUNGU

Tsatanetsane wa mau othandizira pa kusanthula kwa Mau Mulungu

MPINGO UNAKHAZIKITSIDWA NDI MULUNGU

Zoona zenizeni pa mutu wa mpingo zimaunikira chifuniro cha Mulungu ndi cholinga chake pa ife m'moyo uno ndipo zimaaulula kwambiri bodza limene mabungwe achipembedzo amapereka pakati pa anthu. Dzikoli ladzaza ndi zipembedzo zosiyanasiyana komanso mpingo yochuluka imeneno ili ndi miyeso komanso zikhulupiriro zavo zosiyanasiyana. Ngakhale anthu ambiri akumagwirtsa ntchito mfundo yakuti "mukhoza kukapemphera mpingo uliwonse umene inuyo mukufuna", Baibulo limaphunzitsa kuti pali njira imodzi yopapatiza imene imakafika ku moyo (Mateyu 7:13-14).

TANTHAUZO LA 'MPINGO'

Mau akuti *mpingo* akutchulidwa poyamba mu Baibulo pa Mateyu 16:18. "...ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazika Mpingo wanga; ndipo makomo a dziko la akufa sadzagonjetsa uwo." Mau akuti *mpingo* akuchokera ku mau a Chigriki otchedwa *ekklesia* amene atanthauza 'oyitanidwa.' Malemba akugwirtsa ntchito mau akuti *mpingo* kachiwirinso pa Machitidwe 2:47. "...Ndipo Ambuye anawaonjezera tsiku ndi tsiku amene akuti apulumutsidwe." Mpingo si nyumba kapena malo opemphereramo koma wapangidwa ndi anthu amene apulumutsidwa ku machimo awo. Anthu enieni a Mulungu 'ayitanidwa' kuchokera ku uchimo, dziko lapansi ndi zipembedzo etc. iwo ali pa chiyanjano ndi Mulungu ndi umodzi mwa Mzimu, amayenda mu chikhulupiriro cha Mau a Mulungu.

ANTHU OYENERA KULOWA MU MPINGO

WENIWENI WA MULUNGU

Umembala wake suchokera popemphera ndi anthu ena, kapena kulembewda m'dzina lanu mu buku la mpingo wanu, kapena kulandira kalata ya ubatizo. Mulungu yekha amaika anthu mu thupi (I Akorinto 12:18). Tikabwera ku Mpingo wa Mulungu pamene tabadwa mwatsopano, timapulumsidwa ku machimo kudzera mu mwazi woombola wa Yesu Khristu. Aliyense mu Mpingo wa Mulungu akhala wosachimwa.



BUNGWE LAKUMWAMBA

Mpingo si nyumba ayi...
koma umapangidwa ndi
anthu amene apulumutsidwa
ku machimo awo.

YESU NDIYE KHOMO LOKHALO

Yesu ndiye khomo lokhalo lolowera mu Mpingo wake, popeza lye yekha ndiye ali ndi mphamvu yokhululukira machimo "...ngati wina alowa ndi Ine, adzapulumutsidwa..." (Yohane 10:9). Palibe bungwe, wansembe, bishopu kapena mbusa amene ali mphamvu imeneyo. Chifukwa cha ichi, palibe munthu amene angatilowetse mu mpingo ndipo palibenzo munthu amene angatitulutse. Umembala wa Mpingo umasungika kumwamba (Luka 10:20) ndipo maina ake ali m'buku la moyo (Afilipi 4:3). Monga Mulungu amadziwa moyo ndi mtima uliwonse, umembala wa Mpingowu ndi wolondolozeka bwino pa nthawi iliyonse.

KHRISTU NDIYE WOKHAZIKITSA

Mpingo wa Mulungu unakhazitsidwa ndi kumangidwa Yesu Khristu mwini. "...ndi-dzakhazika Mpingo wanga" (Mateyu 16:18). Chipembedzo chilichonse chimene chimaloza kwa munthu ngati wokhazikitsa wake ndi chabodza. Pafupifupi chaka cha 30 A.D., Yesu anakhazikitsa mpingo wake pa dziko lino, osati munthu (Ahebri 8:1-2). Iye anamwalira, naukanso, nakwera Kumwamba ndipo anatumiza Mzimu Woyerwa kuti awapangitse okhulupirira kuti akhale moyo wachiyero.

MAZIKO AKE NDI KHRISTU

Yesu ndiye maziko a dongosolo ili lauzimu. "Pakuti palibe munthu akhoza kuika maziko ena, koma amene aikidwako, ndiwo Yesu Khristu." (I Akorinto 3:11). Mau a Mulungu amene anauziridwa kuchokera Kumwamba ndiwo muyeso wokhawo wa chikhulupiriro mu Mpingo wa Mulungu (2 Timoteo 3:16-17). Malemba ndi wofunkira kwambiri ndipo ali ndi mphamvu yonse pa miyambo, zikhaldidwe ndi zikhulupiriro za anthu. Mu Mpingo wa Mulungu, mulibe bungwe loona za zisankho la ma Bishopu kapena abusa kuti alingalire za tsogolo la mpingo. Mulungu wapereka kale Mau ake ndi Mzimu Wake umene ife tiyenera kukhalira.

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

KHRISTU ALI MLOWAM'MALO

Yesu ndiye "...mutu wa thupi, Mpingowo; ...kuti akakhale lye mwa zonse woyambayamba." (Akolose 1:18). Palibe wina amene angalowe mmalo mwa Khristu kumwamba ngakhale pansi pano.

lye ndiye wa zinthu zonse. "Pakuti Yehova ndiye woweruza wathu, Yehova ndiye wotipatsa malamulo, Yehova ndiye mfumu yathu; lye adzatipulumutsa." (Yesaya 33:22). Mu Mpingo wa Mulungu, mulibe malo, kufunikira kopangira masankho popeza Mbusa ndi Woyang'anira wamkulu, amene ali Khristu, amayang'anira miyoyo yathu.

ATSOGOLERI AMASANKHIDWA NDI MULUNGU

Mu mpingo wa Mulungu, Mulungu mwini amayika anthu

kuti akhale ngati thupi monga mmene wafunira (I Akorinto 12:18). Mulungu amapereka mphatso mu Mpingo (Aefeso 4:10-13) ndipo Mzimu amalongosola ndi kutsogolera zonse molingana ndi chifuniro Chake. Kawirikawiri munthu amafuna kutenga malo amenewa otsogolera ndi kusankha. Mu thupi la Khristu, anthu ake amayang'ana kwa Mzimu Woyeru kuti awatsogolere mu njirayo. Kudzoza ndi utsogoleri sizibwera chifukwa cha maphunziro, kupita ku sukulu ya ubusa, kapena kuhala wachibale wa munthu amene ali ndi udindo koma popatulidwa ku maitanidwe a Mulungu.

MPINGO UNAPATSIDWA DZINA NDI MULUNGU MWINI

Pali maina ambiri ndi maudindo onena za mipingi ndi zipembedzo zimene zinakhazikitsidwa. Komabe Mulungu wawatchula kale anthu ake. "Chifukwa cha ichi ndipinda maondo anga kwa Atate, amene kuchokera kwa lye fuko lonse la m'mwamba ndi la padziko

alitcha dzina" (Aefeso 3:14-15). Ndi chipongwe ku mpingo wauzimu kutchulidwa dzina lina kupatula lokhalo la Atate. Mau a Mulungu amawaphunzitsa abusa "kuti muwete Mpingo wa Mulungu..." (Machitidwe 20:28). Dzina la m'Baibulo la mpingo weniweni ndilo 'Mpingo wa Mulungu'. Mu matchalichi ang'onoang'ono, anthu okhulupirira malemba ankatchedwa kuti Mpingo wa Mulungu

(2 Akorinto 1:1). Kungodziwika ndi dzina lokhali basi sikupulu-mutsa munthu koma limeneli ndilo dzina limene liperekedwa ku mpingo wa Mulungu.

MPINGO UMODZI WOKHA

Mwa mipingi yonse ndi zipembedzo zonse zimene zilipo, Mulungu ali ndi mpingo umodzi basi — Mpingo wa Mulungu. Mpingowu umatchulidwa kuti ndiwo 'thupi la Khristu' (Aefeso 1:22-23). "Pakuti monga thupi lili limodzi, nilikhala nazo ziwalo zambiri; koma ziwalo zonse za thupilo, pokhala zambiri, zili



Mpingo wa Mulungu sulamuliridwa ndi makomiti kapena pochita masankho koma ulamuliridwa ndi Mzimu Woyeru.

thupi limodzi; momwemonso Khristu." (1 Akorinto 12:12). Malemba amanena za mpingo ngati mkwativi (2 Ako-rinto 11:2). Mulungu alibe mitala. Iye anali ndi mkwativi mmodzi ndi mpingo umodzi.

Wowerenga aliyense akhoza kuona kusiyana kwa mpingo weniweni wa Mulungu ndi mipingi ya anthu. The Mpingo wa Mulungu ndiwo mudzi umene umayikidwa pamwamba pa phiri umene sungathe kubisika (Mateyu 5:14). Iwo umakhala pamwamba pa makangano ndi chisokonezo za chipembedzo cha munthu ndi ziphunzitsa. Mpingo wa Mulungu — umene uli wake weniweni wa Mulungu — ndi woyeru, wopatulika, wosadetsedwa ndi woona. Khristu ndiye woukhazikitsa, wotsogolera, wopereka malamulo ndi Mpulumutsi.

-mws



Funso: Mpingo umene ndimapemphera suphunzitsa choonadi chonse chimene chimapezeza mu Baibulo. Kodi nditani?

Yankho: Limeneli ndi yankho lofunikira komanso lolemerera ndipo lifuniika yankho loganizira bwino popeza anthu ambiri akudutsa mu zimenezi. Nkofunikira kuti moyambayamba tidziwe zakuti Mpingo wa Mulungu ndi mpingo wakumwamba. Aliyense amene wapulumutsidwa kuchokera ku uchimo kudzera mwa Yesu Khristu ali gawo la mpingo weniweni (Machitidwe 2:47).

Kupemphera nawo ndi gulu la mpingo uliwonse kapena m'dzina la munthu wina aliyense sikupangitsa kuti munthu wopenpheryo walowa mu mpingo wakumwamba. Anthu amene alapadi machimo awo kwina kulikonse pa dziko lino amalowa mu mpingowu. Iwo amadziona ngati a mu 'gulu' linalake koma izi si zimene Mulungu amaona. Munthuyo ali mu mpingo wa Mulungu kaya akudziwa kapena sakudziwa, popeza Mulungu amaona mu mtima ndi moyo wa munthu.

Bungwe kapena 'mpingo' umene sumaphunzitsa choonadi chonse ukhoza kupangitsa kuti miyoyo ya anthu ambiri iwongeke. Ndi zonna ndithu kuti anthu akhoza kupulumuka chifukwa cha ulaliki ngati pali kulapadi kwenikweni. Vuto la kuitirira kusonkhana ndi mpingo ngati umenewu ndilo lakuti ndi kovuta

kukhalabe 'wopulumuka' chifukwa chinyengo cha zinthu zauzimu chimapangitsa kuti munthu akhalebe pansi pa chipunzitsa chabodza. Palibenzo zokambiranu kuti 'mpingo' umene ukuphunzitsa chinyengo ndipo watayirira pa choonadi cha Mau a Mulungu ndi wakugwa pamaso pa Mulungu. Malemba aku-fanizira mipingoyotereyi ndi Babiloni kapena chisokonezo. Iyo imafanizidwa m'buku la Chivumbulutso ngati 'mahule'. Iwo salola kuti Mzimu wa Mulungu uwatsogolere. Mabuku a zikhulupiriro zaho amaikidwa pamwamba pa Baibulo. Mkumano wa abusa umatenga malo a Mzimu Woyer. Dongosolo lawo ndi lolakwika ndipo



KODI NDIYANJANE NAWO MU MPINGO WACHINYENGO?

Mulungu savomerezana nawo mpingowu. Malemba amaphunzitsa kuti "Turukani m'menemo, anthu anga; kuti mungayanjane ndi machimo ache..." (Chivumbulutso 18:4).

Mdierkezi waononga kwambiri chikhristu ku mipingoyimene imakhlupirira kusiananso ndi zimene wachita kwa osapembedza ndiponso wazunza mpingo moonekera. Mipingoyimene imangophunzitsa gawo limodzi la choonadi koma osati choonadi chonse ndi yoopsa kwambiri kwa anthu amene

akufuna choonadi osangoti chipembedzo chimene chimasiyana ndi zimene Baibulo limanena. Choonadi cha mbali imodzichi chimaperekwa mpata kuti mdaniyo agwire ntchito m'miyoyo ya anthu. Ambuye akufuna kuti tidzipatule pakati pa aneneri onyenga ndi mabungwe okhazikitsidwa ndi anthu ndi kutipangitsa kuti tikhale pa chiyanjano chenicheni cha thupi lenileni la Khristu – umene uli Mpingo wa Mulungu.

Pamene ndondomeko ndi maziko a mipingoyambiri zili zolakwika chifukwa chosaphunzitsa choonadi chenicheni, nkoyenera kuti tizindikire zakuti mu ndondomeko ngati izi muli anthu ena amene ali wolungama. Ngati anthu awa akhala mmoyo wachiyero pamaso pa Mulungu, adzapita kumwamba akadzafa. Koma pamene wina akhala pansi pa chipunzitsa chimene choonadi chake sichili champhumphu, izi zimapangitsa kuti pakupita kwa nthawi, munthu asokonekere. Pamapeto munthu wotere amakhala kakasi nanena – "Kodi ndikhalebe pansi pa chipunzitsa chonyenga ndi kuchilandira, kapena ndikhale womasuka pamaso pa Ambuye ndi kudzisiyanitsa ku izo zimene zili zolakwika?"

Mmene munthu angayankhire mafunso ngati amenewa zikhoza kupangitsa kuti akalowe kumoyo wosatha kapena ayi. Anthu ayennera kuyima nji motsutsana ndi cholakwika ndi kukhala pa chiyanjano cha umodzi wa chikhulupiriro ndi wa Mzimu.

Ambuye atipatse chisomo ndi nzeru zochuluka kwa wina aliyense amene ali mu chipembedzo chonyenga ndi kutipangitsa kuti tikhale nako kulimbika mtima koyima njii pa zabwino ndi zenizeni. Amen.


-mws



KODI MUKUDZIWA?

Machitidwe a Mtumwi Petro

- Dzina lake linali Simoni, mwana wa Yona. Yesu anamusintha dzina namutcha Kefa (Petro), limene litanthauza thanthwe.
- Iye anabadvira ku Betesaida, pafupi ndi Nyanja ya Galileya ndi ntchito yake inali ya usodzi wa nsomba.
- Petro anali mmodzi mwa atumwi 12 oyamba ndipo anali ndi banja.
- Andreyo, mbale wake poyamba anali wophunzira wa Yohane Mbatizi ndipo kenaka anadzakhala mtumwi wo-yamba wa Yesu.
- Iye anamwalira m'chaka cha 64 AD ku Roma pansi pa ulamuliro wa Kaesara Nero. Iye anapachikidwa chozondoka (mutu kuloza pansi) chifukwa amadziona kuti sanali woyenera kufa monga anachitira Yesu.



Jehova-Nisi—Ambuye Mbendera yanga

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.us

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Eksodo 17:15 *Ndipo Mose anamanga guwa la nsembe, nalitcha dzina lake Yehova Nisi:*

Pamene Mose animika manja ake, ana a Israyeli amapambana pa nkhondo yolimbana ndi Aamaleki. Aroni ndi Huri animirira pambali pa Mose nanyamula mikono yake m'malere popeza iye anatopa. Mulungu anaperekira chigonjetso pa mdani wawoyo. Pofuna kuku-mbukira izi, Mose anamanga guwa la nsembe nalitcha dzina lakuti Yehova Nisi limene litanthauza "Ambuye Mbendera yanga."

Asilikali amanyamula mbendera akamamenya nkhondo chifukwa cha zolina zosiyansiyana. Mbendera imagwiritsidwa ntchito pofuna kuwazindikira anthu, komanso pofuna kusonyeza kolowera pa nkhondo, komanso pofuna kuwabweretsa pamodzi asilikali ndiponso ngati chizindikiro cha kupambana. Ana a Israyeli samamenya nkhondo ngati munthu payekha-payekha koma ngati gulu limodzi pansi pa chitsogozo cha Ambuye Mulungu. Yehova anali Mbendera yayo. Aisrayeli anapambana kudzera mu dzina lake.

Nthawi zina utsi ndi fumbi la nkhondo zimapangitsa kuti asilikali asaone bwinobwino. Izi zilinso zoona ndi nkhondo zimene timakumana nazo pa moyo uno. Tikayang'ana kwambiri pakati pathu, tikhoza kufooketsedwa ndi kukhumudwitsidwa ndi zinthu zimene timaziona. TIYENERA kuona pa komanso kuzungulira Mbendera. Khristu ndiye chizindikiro chathu (Yesaya 11:10) ndipo ndi chifukwa cha lye kuti tiyenera kugwira ntchito, kupirira ndi kudzipereka ngati nsembe. Chizindikiro chathu chipezeka mwa Yehova Nisi ndipo ndi mwa lye mmene timapeza cholinga, kulimbi-kitsidwanso ndiponso chipambano.



-mws